

ZITHUNZI: RICHARD FOLOKIYA

Mitengo ya tsanya kwa Bande yomwe idzakhudzidwe

# Mitengo 10 000 ikhudzidwa ndi SVTP

WOLEMBA: MARTIN GELA

Pomwe nthambi ya boma ya Shire Valley Transformation Programme (SVTP) lapereka ndondomeko ya momwe agwirire ntchito m'dera la T/A Mbenje m'boma la Nsanje zadziwika kuti mitengo 10 000 ndi yomwe iononegeko m'deralo.

Mmodzi mwa akuluakulu a SVTP a Arthur Kambombe ndiye adanena izi masiku apitawa pomwe amafotokozera full council ya m'bomalo.

"M'chiringanizo chathu cha Resettlement Plan tapeza kuti ina mwa mitengoyi ndi yachilengedwe pomwe ina ndi yochita kubzala yomwe tikhale tikuidula pofuna kuti tipereke mpata woti ngalande yathu yomwe ndi yotalika makilomitala 118 kuyambira ku Kapichira ku Chikwawa mpaka pa Nkhadzi ku Bangula m'boma la Nsanje," adatero iwo.

A Kambombe adaonjeza kuti akukhulupirira kuti mwandondomeko zomwe ali nazo kontalakitala ndi anthu akuderalo akuyenera kubwezeretsa mitengoyo ndi cholinga choti nkhalango ibwerere m'chimake.

Iwo adati: "Kuonjezera, tapereka mbuzi kwa mabanja ochuluka m'deralo kuti mmalo moti azidula mitengo, aziweta mbuzi komanso ena kukhala ndi nthawi yoweta njuchi m'nkhalangozi."

Mmodzi mwa achinyamata a kwa nyakwawa Bande, a Bande Bande anati pomwe akugwira ntchito yopambanayi a SVTP akuyenera kukhala wosamalitsa.

A Bande adati kuyambira kale m'deralo mitengo ndi chuma chawo chobisika. Mwachitsanzo, iwo adati kwawoko munthu akadula mtengo monga wa tsanya amayenera kupereka chindapusa.

Wapampando wa komiti ya kwa a gulupu Mello a Edwart Banda anati akuyembekezera bwino lomwe ntchito ya ngalande ya SVTP.

A Banda anati: "Tikukambirana kuti tipezeretu mitengo yoti tidzabwezeretse pomwe inayo ikadzaononongeka chifukwatu ife kunoko timakhulupilira kuti tidzikhala ndi mitengo pofuna kupewa ngozi za mphepo komanso kuti magwedwe a mvula akhale abwino ngati kale. Kunotu n'kwa dzuwa tikuyenera kusamalitsa mitengoyi."

Ntchito ya SVTP ikadzatha idzapindulira mabanja 48 400 kuchokera mahekitala 43 370 ndipo iyi ndi ntchito ya zaka 14 yomwe idzathe mu 2031. Ntchitoyi ikugwiridwa ndi unduna wa za malimidwe ndi thandizo la za chuma kuchokera ku boma la Malawi, banki ya padziko lonse ya World Bank, banki ya chitukuko mu Africa (Africa Development Bank), Global Environmental Facility ndi Opec Fund for International Development. ■

## BWALO LA ULIMI



WOLEMBA: ANDREW SAUKANI

# Tcheru ndi El Niño

Kuti dziko lino litha kukhudzidwa ndi ng'amba ya El Niño zisatipatse mantha kwenikweni chifukwa a nthambi ya za nyengo kwathu kuno analosera kale m'mbuyomo kuti zitha kutero.

Izi zikudza pamene a World Meteorological Organisation anatsimikizira kuti pali chiyembekezo 90 peresenti kuti izi zitha kuchitika m'gawo lachiwiri la 2023 kulowa mu 2024 zimene zitsatane ndi kutentha kowirikiza kenaka ng'amba.

Ulimi umasokonera chifukwa mbewu zimapserera m'munda kotero ngakhale ulimi wa mthirira umasokonekeranso. Zirombo zosiyanasiyana monga agulugufe amene amathandizira kuti mbewu zibereke amafa.

Nawonso ulimi wa ziweto umasokonekera chifukwa kumakhala kuti kulibe msipu komanso madzi woti ziweto n'kumamwa zikamva ludzu samapezeka. Ulimi wa nsomba m'maiwe umatheranso pompo kaamba ka kuphwera kwa mitsinje ndi madambo.

Nsomba za mitundu ina zimasamukira kumalo akuya a nyanja potsatira madzi ochepawo. Mitengo m'nkhalango imayoyoka mopanda masamba kotero imalephera kukonza chakudya kenaka imangofota.

Mbalame ndi nyama zina za m'tchire zimene zimadalira mitengo pa chakudya, malo okhala zimasautsika kenako kufa ndi njala. Ng'amba kapena kuti chilala choterechi chimabwezeretsanso ntchito za ukhondo kotero matenda otsekula m'mimba monga cholera amabuka. Chuma kudzera ku ntchito zokopa alendo mphepete mwa nyanja ndi za mtengetenga zimasokonekera.

Kaamba ka nyengo ya El Niño, alimi akuyenera kukhala okonzekera kuti ngati izi zichitike apeze potsamira. Choyambia abzale mbewu zokhazo zopirira ku chilala, zocha msanga kuti ndi mvula yochepa yomweyo adzathe kugwiritsa ntchito chinyezi chochepacho kuti mbewu zikule mpaka kufikira pobereka.

Alimi musachite kudikira kuti mvula igwe kawiri kapena katatu musanabzale chifukwa potere kumakhala kuti mbewu za amene anabzala moyambirira zikutha msinkhu. Alimi tisachedwe kuganiza zomadzakonza minda yathu mvula ili mkati.

Ndipo onetsetsani kuti mwapanga mabokosi ogwira madzi m'minda (box ridges) kapenanso zigwembe zokola madzi m'minda kuti chinyezi chikhale chokwera.

Njira ina imene ikufunika kulimbikitsidwa mkati mwa chiopsezo cha El Niño ndi kukolola madzi. Alimi atha kukhala ndi mathanki kapena kukumba pansi n'kumakololapo madzi. Kumene kuli madambo onetsetsani kuti mwatchinga madzi kuti asamangopita kumtsinje koma izi zichitike mosamala kuopetsa kusefukira kwa madzi.

Alimi musalime mbewu za mtundu umodzi pozindikira kuti mbewu zimakhudzidwa mosiyanasiyana ndi ng'amba kotero mutha kupulumukira ku zina zimene sizimakhudzidwa kwambiri ndi chilala. Ngati n'kotheka gulani inshulansi ya Mtetezi wa mbewu kuti zikachitika mudzaone potsamira.

Ngati zinthu ziri chonchi, alimi samalani pa kagwiritsidwe ntchito ka chakudya chimene mwasunga kuti chidzalumikizane ndi chimene chingadzakololedwe chaka chino. Pomaliza tiyeni tiliikize dzikoli m'mapemphero pamene tikuyang'anizana ndi nyengo zosautsa zoterezi. ■

*Mafunso: saukaniandrew@gmail.com*